Rural Poultry Centre Malawi

PO Box 81
Likuni
Malawi
Tel: +265 (0)995 943034
Email: rpc@ruralpoultrymalawi.org
Web: www.ruralpoultrymalawi.org

CHIDZIWITSO
MATENDA A KUTUPA MASO KOMANSO MUTU KU NKHUKU

Pali matenda otchedwa korayiza amene amaoneka ku nkhuku za kumidzi. Matendawa amatchedwanso *chikwirikwiti* kapena *chinfine cha nkhuku*. Amaoneka kawiri kawiri ku nkhuku za kumudzi. Akhoza kupha nkhuku zambili, makamaka nkhuku zazikulu, ndipo zazing'ono zimadwalanso koma zochepa.

Maonekedwe a Matendawa

- Zizindikilo: Kuyetsemula, kubanika, m'maso kukha misozi ndipo masowo amatupa, kutuluka mamina kapena madzi m'mphuno, m'kamwa ndi m'mphuno za nkhuku mumanunkha.
- Maonekedwe a ziwalo: M'maso ndi m'mphuno mumatuluka mafinya oyera kapena achikasu.
- Matendawa amayamba mwadzidzidzi komanso angathe kuyamba pang'ono pang'ono. Matenda amenewa amagwira m'mpuno ndi malo ena amene amathandiza kupuma. Amatupitsa malo ozungulira m'maso ndi mutu wonse. Amayambitsa kutsokomola ndi chifine.
- Nkhuku zingathe kudwala matendawa kwa sabata limodzi kapena kupitililapo. Nkhuku zikhoza kufa ndi matendawa.

Chithunzi : Zizindikilo za matenda a Korayiza (Kusonyeza mutu ndi maso otupa. Credit: Cornell Univ.)

Choyambitsa

- Kachirombo kamtundu wa "bacteria" kosawoneka ndi maso, kamene kamapezeka kwambiri muno m'Malawi.
- Chiyambi cha matendawa: Nkhuku zimapatsirana kuchokera ku madzi kapena mpweya umene zimapumarana, osaiwaranso m'chakudya.

Kuchiza

- Mankhwala a *sulfathiazole* kusakaniza ndi zakudya kapena mankhwala a *sodium sulfathiazole* kusakaniza mu madzi akumwa; kapena kupereka ma antibiyotiki.

Kupewa

- Ndikovuta kuteteza matendawa ku nkhuku zoyendayenda chifukwa zimakumana ndi nkhuku zochokera ku malo ena. Ndikotheka kuteteza matendawa ku nkhuku zodyera m'khola poteteza nkhuku zina zodwala kubwera pafupi.
- Nkhuku zosiyana misinkhu zisakhalire pamodzi, ndipo nkhuku zokalamba zichotsedwe kapena zigulitsidwe kupewa kupatsa matenda kunkhuku zazing'ono.

Board of Trustees – Chairperson: Prof T N Gondwe
Members: Dr P Chikungwa, Dr G R Njunga, Mr B Lwara, Mrs J Kanyama-Chikoti